MATEMBERERO AKUMTUNDU (M'BADWO)

MLEMBI: Ken Paynter
OMASULIRA MCHICHEWA: David Makiyi)

CHIKHRISTU CHOSAIMA PACHOONADI CHIFUKWA CHA MANTHA AZIPHUNZITSO ZOSADZIWIKA.

Tiyeni tione za mutu wa chiphunzitso chathu " mantha a akhristu" kapena ena mwa ife kukhoza kukhala kovuta kuti tibvomereze kuti aKhristu ambiri ali amantha. Koma miyezi ingapo yapitayi ndakumanapo ndi aKhristu ambiri amene atengeka mtima ndi chiphunzitso chakuti" matemberero amadzera mmagazi akumtundu wako kapena kuti makolo ako.

1. Nthawi zambiri anthu amakhala ndichidwi ndi zinthu zooneka zodabwitsa kapena zazikulu monga kuonera masewero olawula kapena ogwiritsa mau achipongwe (spooks) kapenanso masewero owonetsa za matsenga "goblin" Anthu ambiri amakhala otengeka mtima pazinthu ngati zimenezi.

2. Kachiwiri anthu ambiri amaika zofoka zawo ndikulephera kwawo pa anthu ena kapena chimo lawo pa zinthu zina. Mmaganizidwe amasiku ano, anthu salolera kubvomereza zolokwa zawo. Pena timakhoza kuika kulepheraku pa bambo athu, mayi athu abale athu kapenanso dera limene tiri kukhala. Izi ndi zimene tiri, zidayambira kutari mbuku la Genisesi pakulengedwa kwamunthu. Adamu adaloza chala Hava ndipoHava adaloza chala njoka koma njoka inalibe woti iloze, inalibenso miyendo yoti iyimilirepo. Munthu sanafuna kulorera kulephera kwake.

Chipulumutso chophatikizirapo "chinachake"

Chinthu ichi chotchedwa themberero chiri ndi maonekedwe amakopedwe kwa anthu ambiri. Nthawi zambiri anthu amene atembenuka mtima magulu aanthu akuda khungu amene anali kupembeza mizimu ya makolo awo amene anafa, amalozedwa chala kuti iwo amabweretsa ziwanda muchipembedzo cha Chikhristu. Koma sitirikuchita bwino pamene tiri kubweretsa zinthu zachilendo komanso mantha muchipembedzo chathu cha Chikhristu, pakuchititsa kuti anthu ena akakaiyike kuti mwazi wa Yesu umene

unaperekedwa kukhala nsembe yotitsukira machimo athu, kuti singathenso kutimasura kuzinthu za kale lathu. Ichi chotchedwa “chapadera kapena chinachake” kuti munthu akadutsenso mumadongosolo ene kapena kukawonana ndi munthu wina amene ali ndi kuthekera kwa maphunziro ena; kuti akatimasure kumzere wamatemberero ochokera kumtundu wathu kapena kuti makolo athu chiri kuphwanyidwa ndi mau aMulungu opezeka pa 1 Akorinto 5:17 mau Amulungu akuti:

- “Chifukwa chake ngati munthu aliyense ali mwa Khristu ali wolengwedwa mwatsopano; zinthu zakale zapita taonani zakhala zatsopano”

M’zaka zambiri zapitazo panalinso chiphunzitso china chimenenso chimapangitsa kuti anthu asatenge udindo wa kubvomereza kulakwa kwawo ichi chinali chiphunzitso chonena kuti “Mkhristu wodzala ndi ziwanda” Anthu anali kupemphereredwa kuti ziwanda za fodya komanso za kachaso zituruke mwa iwo. Pali ponse pamene umayang’anapoi ziwanda za fodya komanso zamowa zinali yakali yakali kuturuka. machitidwe achilendowa analowa mu mpingo kwa zaka zambiri. Mawu aMulungu akuti tiyenera kukhala akulu m’sinkhu, kuti tisatengedwe ndi mphepo yaziphunzitso zosiyasiyana. Komabe timaona kuti mumpingo muli chiphunzitso china chatsopano, ndipo chiri kuikizidwa kwa aKhristu. Chimaiikizidwa kwa anthu amene sadziwa choonadi cha mau aMulungu, anthu amene alibe maziko enieni amau aMulungu. Akhristu ambiri lero sawerenga Baibulo (mau aMulungu) ndipo kwa iwo amene amawerenga, amawerenga vesi immodzi, kapena amagwiritsa ntchito Baibulo pofuna kupeza maumboni andime zina zimene iwo awerenga kuchokera mmabuku ena. Koma ndi aKhristu ochepa amene amawerenga Baibulo molitsatira bwino. Ichi ndi chifukwa chake ziphunzitso zotere zimapeza malo mitima komanso m’miyoyo yawo.

KODI MKHRISTU WOTEMBENUKA MTIMA ANGAKHALE WODZALA NDI ZIWANDA?

Pakubwera ku funso lonse lakuti; kodi Mkhristu wotembenuka mtima mkukhala wodzala ndi ziwanda? 2 Akorinto 6:14 mau aMulungu akuti:

- Musakhale omangidwa m’goli ndi osakhulupirira osiyana; pakuti chilungamo chigawana bwanji ndi chosalungama? Kapena kuunika kuyanjana bwanji ndi mdima? Kapena Khristu abvomerezana bwanji ndi Beliyali? Kapena okhulupirira ali nalo gawo lanji pamodzi ndi osakhulupirira? Kapena chiphatikizo chake chanji ndikachisi wa Mulungu ndi wa mafano?

Tsopano ichi ndi chiletso kapena lamulo kwa ife kuti sitiyenera kukwatirana ndi osakhulupirira kapena kuchita chiyanjano ndi osakhulupirira. Kapena kuunika kuyanjana bwanji ndi mdima? Koma anthu ali ndi chiphunzitso chakuti ziwanda zikhoza kukhala mwa munthu wokhulupirira. Kodi Mzimu Woyera amene amatilimbikitsa kukhala mmoyo wa chiyero akhoza kukhala pammodzi ndi ziwanda? Ndikhulupirira kuti izi sizoona.

DZINA LA YESU

Tsopano ndiri kukhudza zina mwa zithumwa za Chikhristu za mwayi, zimene akhristu amagwiritsa ntchito.

Chithumwa choyamba ndi dzina la Yesu; Tsopano mukhoza kuyamba kudabwa kuti ndaika dzina la Yesu ngati chithumwa, koma anthu ambiri amagwiritsa ntchito dzina La Yesu chotero. Ambuye Yesu sanatipatse dzina lake; koma mphamvu ya dzina lake- ndipo pali kusiyana kwakukulu pakati pa zinthu ziwirizi. Panali ana asanu ndi awiri a Skeva mbuku la Machitidwe amene anayesera kuturutsa ziwanda mdzina la Yesu, ndipo iwo adati “mdzina la Yesu amene Paulo alikulalikira – turuka” Koma munthu waziwandayo anawayankha kuti.

- “Yesu timudziwa, Paulo timamudziwa koma inu ndinu ndani?”

Kenako munthu waziwandayo anawagwera nawamenya kwambiri – ndipo iwo anathawa zovala zawo ziri zong’ambidwa komanso atapwetekedwa, magazi ali chu! Chu! Chu. Chifukwa chiani? Yesu sanatipatse dzina lake koma anatipatsa mphamvu za dzina lake. Kuti ukhale ndi mphanvuyi uyenera kukhala munthu omvera Mulungu. Mau aMulungu amati: “Mkanizeni mdyerekezi ndipo adzakuthawani” Ndipo iwo amaganiza kuti malembawa amathera pomwepo. Nanga kodi malembawa amatanthauza chiani?

- “Potero mverani Mulungu; koma kanizani mdyerekezi, ndipo adzakuthawani.” (Yakobo 4:7)

Ungathe kumukaniza mdyerekezi mmene ungathere, koma ngati ndiwe munthu osamvera Mulungu satana sangakuthawe. Kenturiyo amene anatumiza mau kwa Yesu akuti mwana wake wadwala ndipo amafuna thandizo la Yesu, anati: “pakuti inenso ndiri munthu wakumvera ulamuliro,” Sadati: “ndine munthu wa ulamuliro” koma kuti:

- “Pakuti inenso ndiri munthu wakumvera ulamuliro, ndiri nawo asilikali akundimvera ine: ndipo ndinena kwa uyu “muka” Namuka, ndi kwa wina “idza” nadza; ndikwa kapolo wanga ‘chita’ nachita. (Mateyu 8:9)

Mukuwona, kuti ukhale ndi Ulamuliro uyenera kukhalanso pansi pa ulamuliro- ndiye ukhoza kukhala ndi ulamuliro pa mdyerekezi, tiyenera kukhala pansi pa ulamuliro. Pali anthu ambiri amene sali pansi pa ulamuliro. Sali pansi paulamuliro wa Uzimu wa chipembedzo wa pa mpingo wapamalo, salinso pansi pa ulamuliro wa mmabanja awo. Ngati ife sitiri pansi pa ulamuliro ndiye kuti tiribe ulamuliro.

KULENGEZA MWAZI, ENA AMATI: (KUWAZA MWAZI)

Chithumwa china chopatsa mwayi ndicho Kuwaza kapena kulengeza mwazi wa Yesu. Kuwaza kwa mwazi uku kunachitika Mchipangano chakale, ena alikukugwiritsabe ntchito koma siziri kufanana ndi mmene zinachitikira Mchipangano chakale. Anthu

amawaza mwazi pamyumba zawo chuma chawo mzipinda zawo. Kuwaza mwazi kwa Mchipangano chakale kunali kutetezera anthu ku mkwiyo wa Mulungu osati kumphamvu zasatana.

- “Exodus 12:13 Ndipo pamene ndiona mwaziwo ndidzapitirira inu:

Pamene tiika mwazi wa Yesu pamoyo wathu, umatitetezera ku mkwiyo wa Mulungu. Iwo amene alibe mwazi wa Yesu padzitseko za mtima wawo adzakomana ndi mkwiyo wa Mulungu, chifukwa mwazi waYesu ulipo kuti ukatitetezere. Osati kwa satana koma ku mkwiyo wa Mulungu. Anthu ena amatenga mbali immodzi ya lemba ndikuitanthauzira njira yawo osati monga mmene iliri. Ndikhulupirira kuti mau amene anthu amakonda kugwiritsa ntchito ndi ochokera ku buku la Chibvumbulutso 12:10-11 Ndipo ndinamva mau akulu mwamba, nanena, tsopano zafika chipulumutso, ndi mphamvu, ndi za ufumu wa mulungu wathu, ndi ulamuliro wa Khristu wake, Pakuti wagwetsedwa wonenera wa abale athu, wakuwanenera pamaso pa Mulungu wathu usana ndi usiku. Ndipo anamlaka iye ndi mwazi wa mwana wa Nkhosa, ndi chifukwa cha Mau amaumboni awo. Tingathe bwanji kugonjetsa zotitsutsa? Komatu ndi mwazi wa Yesu. Pamene iye atiuza za mmene tinaliri ochimwa timamugonjetsa ndi mwazi wa Yesu. Mwazi wa Yesu umatichotsera machimo athu onse, ndi mmene timagonjetsera ndi maumboni awo: osati zithumwa chifukwa mawuwo akupitiliza kunena kuti: Ndipo iwo anamlaka iye chifukwa cha mwazi wa mwana wa nkhosa, ndi chifukwa cha mau aumboni wawo, ndipo sakonda moyo wawo kungakhale kufikira imfa. Anthuwo anali okonzekera kufa chifukwa cha chikhulupiro chawo ndi mmene adamugonjetsera mdyerekezi.

KUMANGA NDI KUMASULA

Kumanga ndi kumasula, ndi chithumwa china chimene anthu enanso amagwiritsa ntchito. Mbuku la Mateyu 16:18-19 mau aYesu anati:

- “Ndiponso ine ndinena kwa iwe, kuti iwe ndiwe Petro, ndipo pathanthwe ili ndizakhazika mpingo wanga; ndipo makomo adziko la akufa sadzaulaka uwo. Ndidzakupatsa mafungulo a Ufumu wa kumwamba; Ndipo chimene ukamanga pa dziko lapansi chidzakhala chomangidwa kumwamba; Ndipo chiri chonse ukachimasula padziko lapansi, chidzakhala chomasulidwa kumwamba.

Ndiponso ine ndinena kwa iwe kuti iwe ndiwe Petro “petros” - mwala wa ung’ono “…Ndipa Thanthwe ili “ Petra” - Thanthwe ili - Thanthwe lachibvomerezo chako ndidzakhazika mpingo wanga. Petro sindiye mazikowo monga aKatolika amaphunzitsira. Chibvomerezo cha Peturo ndimaziko amene Yesu amamanga mpingo. Baibulo limanena kuti:

- Kuti ngati udzabvomereza mkamwa mwako Yesu ndi Ambuye, ndikukhulupira ndi mtima wako kuti ambuye anamuwukitsa iye kwa kufa, udzapulumuka. (Aroma 10:9)

Ndidzamanga mpingo wanga ndipo makomo adziko la akufa sadzaulaka.

Mau oyamba achiGreek- makomo a imfa sadzaulaka iwo; Hade simalo amene satana alikukhala tsopano. Hade ndi malo amene okhulupirira oyamba anali kupita Ambuye Yesu asanafe, komanso akufa ochimwa anali kupita komweko. Mukhoza kuwona zimene Ambuye Yesu ananena zokhuza malo otchedwa Hade, Ambuye Yesu ananena kuti mwini chuma adamwalira ndipo anapita kumalo otchedwa Hade, pamene Lazaro wa umphawi atamwalira, anatengedwa kukhala pa chifuwa cha Abrahamu, Chifuwa cha Abrahamu linali gawo limodzi la Hade; chifukwa mwini chumayi anali kumuona Lazaro wa umphawi, ndiponso anampempha iye timadzi ta kumsonga la lilime lake. Onsewa anali ku Hade koma panali pompho lakuwasiyanitsa awiriwa kuti wina sangathe kupita mbali ina.

Pamene ambuye adanena kuti makomo adziko la akufa sadzaulaka mpingo wa Yesu, Iye anali Kunene za mpingo wake wa Mchipangano Chatsopano umene sudzadutsira pa makomo aku Hade. Anthu aMchipangano cha Kale amayenera kudutsira ku Hade chifukwa Ambuye Yesu anali asanafe pamtanda komanso anali asanalipire mtengo wake wa machimo athu, ndi chifukwa chake anthu aMulungu akamwalira nthawi imeneyi anali kupita ku Hade. Koma Baibulo likunena kuti Yesu Khristu ali nazo zifungulo (makiyi) za imfa ndi Hade. Yesu anati Chibvumbulutso 1:18:

- “Ndili wa moyoyo, ndipo ndinali wakufa, ndipo taona ndiri wa moyo kunthawi za nthawi, ndipo ndiri nazo zifungulo za imfa ndi Hade,

Aefeso 4:7-8 ali kunena kuti:

- “Ndipo kwa yense kwapatsidwa chisomo, monga mwa muyeso wa mphatso ya Khristu, chifukwa chake ananena; mmene anakwera kumwamba, anamanga ndende undende, Naninkha za ufulu kwa anthu.”

- (Komai chi chakuti anakwera mchiani nanga, koma kuti anatsikiranso kumadera akunsi kwa dziko? Iye wotsikayo ndiye Yemweyonso anakwera, popitiriratu miyamba yonse, kuti akadzaze.) (Aefeso 4:9-10)

“Ndiye kuti pamene Yesu anafa anatsikira kunsi kwakufa..” Yesu anapita ku Hade “pachifuwa cha Abrahamu kapena kuti ku Paradiso” osati ku gahena. Iye sanamenyedwe kapena kuzunzidwa ndi ziwanda, (ngakhale kuti ziwandazo panopa siziri ku gahena) kapena kulavuliridwa ndi zina zotero. Ichi ndi chiphunzitso chopanda tanthauzo, chosagwilizana ndi malemba chimene chakhala chikuyenda mzaka zingapo zapitazo. Yesu anamuuza wambanda wopachikidwa pamtanda uja kuti, “ “Ndipo iye ananena naye, Indetu ndinena ndi iwe Lero lino ukakhala ndi ine mparadiso.” (Luka 23:43) “Iye anatinso, adakali pamtanda kwatha” (John 19:29) Ndipo nsalu yotchinga ya mkachisi inang’ambika pakati, kuonetsera kuti njira yolowera ku malo opatulikitsitsa inatseguka. (Matt 27:51) Mau achipulumutso adakwaniritsidwa, dipo la machimo athu linalipiridwa. Padalibe chifukwa choti Yesu apitire ku gehena kukazunzidwa ndi ziwanda monga ena

amaphunzitsira. Ngati sitidziwa malemba ndikosavuta kugwa muukonde wakukhulupira mabodza amene anthu ena amaphunzitsa mu mpingo.

Pamene Yesu anatsikira kwakufa, analalikira kwa iwo amene anali omangidwa uthenga wabwino ndipo pamene iye anakwera Baibulo limanena kuti Iye anawatsogolera akumangidwawo. Chifuwa cha Abrahamu (paradise) sichirinso padziko lapansi. Kumbukirani kuti pamene Yesu adapachikidwa pamtanda adati kwa chigawenga chija chimene chidalapa kuti, “Lero ukakhala ndi Ine Mparadiso wa Atate wanga” Kodi Yesu amapita kuti? Sanali kukwera ; anali kutsikira kwakufa. Chifukwa Iye adati:

- “Pakuti monga Yona anali mmimba mwa nsomba masiku atatu ndi usiku wake, chomwecho mwana wa munthu adzakhala mumtima wa dziko lapansi masiku atatu ndi usiku wake.” (Mateyu 12:40)

Paradiso anali kunsi kwa dziko, koma mu buku la 2 Akorinto 12:4 Paulo adanena za ku “kwaturidwa mparadiso.” Paradiso Salinso kunsi kwa dziko; paradiso ali kumwamba chifukwa dipo la machimo athu linalipiridwa ndipo onse amene anali ku Hade adamasulidwa.

Ndipo Yesu alikunena mosimikiza kuti, “Ndidzamanga mpingo wanga pachibvomerezo chakuti Yesu ali Ambuye – ndipo mpingo uwu sudzapita ku Hade.” Ndipo makomo adziko la akufa sadzaulaka. Makomo aku Hade adapondereza iwo aMchipangano cha Kale, koma sakhoza kupondereza iwo aMchipangano cha Tsopano. Anthu amalankhula za mdyerekezi ngati ali kale mmoto wa gehena, omatutu munyengo ino iye sali ku gehena. Anthu ali ndi malingaliro akuti mdyerekezi amazunza anthu ku gehena. Anthu amatenga zinthu izi m’masewero, koma simungathe kuzipeza mmawu aMulungu. Kodi mungathe kundipezera Mmawu aMulungu Mbaibulo amene amanena kuti, inde! Ndikudziwa za anthu akufa amene amabwerera kwa kufa ndikumafotokozera za mabvumbulutso odabwitsa azinthu zimene zinachitika. Abale sitiika chiphunzitso pazimene munthu alikunena zimene siziringana ndi mau aMulungu. Sitikhazikitsa chiphunzitso pa maumboni a anthu kapena masomphenya aanthu, timakhazikitsa chiphunzitso pa Mau a Mulungu.

Baibulo limatiuza kuti satana ndiye “mfumu ya dziko lino lapansi” (Yohane 12:31, 14:30 & 16:11) iye ndiye “wolamulira wa mlengalenga (Aefeso 2:2). Mbuku la chibvumbulutso limanena kuti munthawi ya chisautso iye adzatayidwa kuchoka kumwamba kumene iye alikuneneza abale ku mpando wachifumu wa Mulungu usiku ndi usana. Ngati satana alindikuthekera kopita kumwamba kukamvetsera pa khutu la Mulungu iye sangamataye nthawi yake kumapita ku gehena kumakazunza anthu. Nthawi idzafika imene iye adzaponyedwa padziko lapansi (Chibvumbulutso 12) adzamangidwa ndikuponyedwa Mudzenje la mdima yotchedwa (Abyss) (Chibvumbulutso 20). Chinthu chimodzi choopsa chokhudza nthawi ya chizunzo ndi chakuti Iye amene ali woletsa wa nthawiyi adzachotsedwa (2 Atesalonika 2:7). Kodi ndani ali woletsa uchimo m’mudziko lino lapansi? Ndiye Mzimu Woyera. Kumbukirani pamene Ambuye Yesu adanena kuti Atate adzatuma Mzimu Woyera amene adzakhala ndi ife kunthawi zosatha (Yohane 14:16). Ngati Mzimu Woyera atengedwa kuchoka kudziko lapansi, inu nokha mukudziwa wina

ndani amene ayeneranso kuti atengedwe? Mpingo! Ndiye kuti m'nthawi ya chisautso chachikulu sudzakhala uli padziko lino lapansi, mpingo wa Yesu udzakhala utakwatulidwa. Pamenepo Mulungu adzatsanulira mkwiyo wake padziko lapansi ndipo chinthu choopsa kwambiri ndichakuti ziwanda komanso satana adzakhala alikugwira ntchito padziko lapansi –kopanda Mzimu Woyera kuwaletsa iwo chinthu choopsa kwambiri, dziko loipitsitsa limene lidzaoneke mnthawi imeneyi. Ndiri wa chisoni ndi wanthu amene adzatsare pakukwatulidwa komanso iwo amene adzachite nayo nthawi iyo.

Ngati "kumanga ndikumasura", ndi "kuwaza mwazi" ziri zida zamphamvu zomenyera nkhondo yathu ya uzimu, chifukwa chiani Atumwi a Yesu sanazigwiritse ntchito? Mutandipezerako nthawi immodzi imene Mtumwi Petro kapena imene Mtumwi Paulo "anawaza waza mwazi wa Yesu" kapena pamene iwo "anamanga ndi kumasura" Ndipo zida zachilendo zimenezi aKhristu ambiri anthawi ino alikugwiritsa ntchito munkhondo ya uzimu. Zida Zimenezi siziri mundandanda wa zida za nkhondo yathu zimenene zinalembedwa mbuku la Aefeso 6 pamene pali zida za Mulungu.

Tsopano zokhuza "kumanga ndi kumasura" mabaibulo amatanthauzidwe amchingerezi awa alikunnena kuti: KJV

- "chiri chonse chimene mudzachimanga padziko lapansi, chidzakhala chomangidwa kumwamba; Ndiponso chiri chonse chimene mudzachimasula padziko lapansi chidzakhala chomasuridwa kumwamba." (Mateyu 18:18)

The New International Version:

- "Ndinena choonadi, chiri chonse chimene mwamanga padziko lapansi, chidzamangidwa ku mwamba, ndipo chiri chonse mwamasula padziko lapansi chidzamasulidwa kumwamba"

Ndemanga za ndime za mmusi zamatanthauzidwe a NIV zimaonetsera kuti; "chidzamangidwa" angatanthauziridwenso kuti "zinamasulidwa" Young's Literal Translation amanena kuti:

- "…Chiri chonse chimene mudzamanga padziko chidamangidwa kumwamba, ndi chiri chonse chimene mudzamasula padziko chidamasulidwa kumwamba."

Ndime za Mateyu 16:19 ndi 18:18 zimagwiritsa mneni wakewake wochokera ku ChiGreek okhala ngati owenetsera za mtsogolo (periphrastic future perfect). Anatanthauziridwa bwino m'matanthauziridwe a NASB (New American Standard Bible): [1]

- "Chiri chonse chimene mumanga chinamangidwa mwamba ndi chiri chonse chimene mumasura chinamasulidwa kumwamba."

[1] Grudem W, Systematic Theology, Zondervan, 1994

Ndiye kuti kumanga ndi kumasula kwa Mulungu kumwamba kumakhala koyambirira kubwera kusanadze kumanga ndikumasula kwa mpingo. Machitidwe ampingo padziko lapansi amaoonetsera chiweruzo cha Mulungu kumwamba. Mpingo umatsatira Mulungu osati Mulungu kutsatira mpingo. Uku ndiye kutanthauzira kwenikweni kwa kumanga ndi kumasula. Afarisi analinso kugwiritsa mchitidwe wakumanga ndi kumasula pakuwauza anthu zinthu zimene zinali zoloredwa ndizosaloredwa. Zimene Ambuye Yesu anali kuchita anali kutsatira. Mpingo wa nthawi ineneyo unalibe mabaibulo monga mmene ife tili nawo. Inu ndi ine tiri ndi Baibulo lonse, mpingo woyamba unali ndi Buku lachipangano chakale la(Chilamulo cha Mose ndi Aneneri.) Analibe Buku lachipangano chatsopano koma anali kulowa nyengo yatsopano ya Chisomo, imene zinthu zina ukhoza kuchita monga ungawonere ayi! Ambuye Yesu adati kwa Atumwi:

- “Ndakupatsani ulamuliro, ndakupatsani zifungulo, chiri chonse chimene muchibvomereza, chidzabvomerezedwa, ndipo chilichonse muchikaniza chidzakanizidwa.”

Kuterotu basi. Monga aFarisi anali kumanga ndi kumasura, Ambuye Yesu anapereka mphamvu kwa Ophunzira ake zakumanga ndikumasura. Iwo sanapita pita mmalo ozungulira kukamanga kapena kukamasura mdyerekezi ndi amithenga ake. Satana adzamangidwa kwa chaka chikwi kundende ya m’dima ya Abyss Rev 20 koma kufikira kunthawi imeneyo Iye ali kuyenda yenda monga mkango wobangula kufuna wina umulikwire. Palibe chimene iwe ndi ine tingathe kuchite-palibe uthenga wa Uzimu umene iwe ndi ine tingachite kuti timuletse iye. (1 Petro 5:8).

Tingathe kuletsa machitidwe ake oipa mmoyo mwathu, komanso maanja athu, chifukwa pali mbali ina ya chichiyeretso imene imabwera mwa okhulupirira ngakhale atakwatira munthu osakhulupirira. (1 Akorinto 7:14) Ambuye Yesu anali kungonena kuti sichorandirika kwa onse. Anthu asangonene kuti “sitiri pansi pakumvera lamulo ndipo ndingathe kuchita chiri chonse chondikondweretsa” Atumwi anali ndi zifungulo za ufumu zokhoza kunena chimene chakanidwa kapena chimene chabvomerezedwa. Ndipo tiri kuona kuti iwo adagwiritsa ntchito Ulamuliro wawo. Mau a Machitidwe Atumwi 15:28-29 ali kunena kuti pamene Atumwi anakumana ndi funso lokhudza mdulidwe iwo anati:

- “Pakuti chinamkomera Mzimu woyera ndi ife, kuti tisasenzetse inu chothodwetsa china chachikuru choposa izi zoyenerazi; kuti musale nsembe za mafano, ndi mwazi, ndi zopotola, ndi dama; ngati muzisungitsa pa zimenezi, kudzakhala bwino kwa inu. Tsalani bwino.”

Ndipo mukudziwa chiani? Anamasulidwa kwambiri patsogolo pa nthawi. Paulo analembera kalata mpingo wa ku Akorinto kuti nnati ali kudya nyama yogulitsidwa pa msika, ndipo ngati Sali kudziwa kuti iri yoperekedwa kumafano, asadandaule zachimenechi.

- **Idyani nyama iriyonse yogulitsidwa pamsika kopanda kukhala ndi funso la chikumbumtima Dziko lapansi ndi la Yehova ndizolengedwa zonse ziri**

momwemo. Ngati wina osakhulupirira akuitanani, ndipo mufuna kupita; Mudye chomwe chaikidwa kwa inu, osafunsa kanthu chifukwa chachikumbumtima. Koma ngati wina akati kwa inu, yoperekedwa nsembe iyi, Musadye, chifukwa cha iyoyo wakuuza, chifukwa chachikumbumtima. Ndinena chikumbumtima, sicha iwe mwini, koma cha winayo; pakuti ufulu wanga uyesedwa ninji ndi chikumbumtima cha wina? Ngati ine ndilandilako mwachisomo ndi nenezedwa bwanji chifukwa cha ichi ndiyamikako? (1 Akorinto 10:25-30)

Pamene mpingo udakula okhulupirirawo adamasulidwa kuzinthu zambiri, koma poyambirira mpingo unauzidwa kuti usadye myama imene yaperekedwa nsembe kumafano. Patapita nthawi yayitali Paulo anakumbutsanso mwa ulamuliro ;okhulupirira kuti asadye nyama iriyonse yoperekedwa ku mafano. Uku ndiye kumanga ndi kumasura. Kumanga ndi kumasula kunaperekedwa kwa Atumwi kuti akayankhure mwa Ulamuliro za zinthu zimene ziri zoloredwa ndi zosaloredwa.

Matemberero akumtundu

Tiyeni tibwere kumatemberero akumtundu Deuteronomy 5:9 ndi kumene izi zinayambira komanso zinatchulidwanso mbuku la Eksodus 20. Maverse awiri onsewa ali olumikizidwa ku malamulo khumi amene anaperekedwa kwa Mose. Pa Deuteronomy 5:9 pali mau akuti:

- “….. Wakulanga ana chifukwa cha atate awo, kufikira M’badwo wachitatu ndi wachinayi wa iwo amene akudana ndi ine.”

Zimene siziunikiridwa bwino mundime imeneyi ndi zakuti matembererowa adzafika pa iwo akudana ndi Mulungu.. Chisalungamo ndi tchimo limene limaonekera pa mlingo wina wapatsogolo. Mbuku la (Yesaya 53:5) mau aMulungu amanena kuti: Koma Iye analasidwa chifukwa cha zolakwa zathu, chinthu chimmodzi tiyenera kudziwa bala silimangoonekera nthawi immodzi. Wina akhoza kukumenya pa mkono wanu, ndipo inu mutayang’ana nthawi zina simungathe kuwona china chiri chonse. Tsiku lina mutayang’ana mukhoza kuona kuti pali bala; umo ndi mmene chosalungama chimakhalira. Ndi tchimo limene liri m’banja mwako, kuti ngati sutumikira Mulungu limaonetseredwa mmuyo wako. Mungathe kuona kuti ngati m’banja mwamuna amakonda kumenya mkazi wake ananso amuna am’banjalo adzamenyanso akazi awo. Ngati makolo amakonda kumwa mowa ananso amakhala okonda mowa. Pali kuthekera kochuruka kuti mwana akhoza kutengera, kuchita zimene kholo laqke limachita. Ngati mudana ndi Mulungu.

Tidziwe kuti chosalungamachi chidzafikira m’badwo wa chitatu ndi wa chinayi wa iwo akudana ndi Mulungu. Ichi chikutipangitsa ife kuzindikira kufunikira kwa zochita za makolo pa miyoyo ya ana awo. Izi ndizofunikira kwambiri. Ayuda adayamba kukhulupirira kuti ngati china chake chalakwika pamayo wawo ndiye kuti atate wawo anachimwira Mulungu. Ngakhale mthawi ya Ambuye Yesu mbuku la Yohane 9, anthu anali kukhulupirirabe kuti cholakwika chimachokera kwa makolo.

Muli nkhani yokhuza Yesu ndi ophunzira ake:

- Ndipo popita, anaona munthu ali wosaona chibadwire. Ndipo akuphunzira ake anamufunsa iye, nanena, “Rabi, anachimwa ndani, ameneyu kapena atate ake ndi amake kuti anabadwa wosaona? Yesu anayankha sanachimwa ameneyu, kapena atate wake ndi amake, koma kuti ntchito za Mulungu zikaonetseredwe mwa iye. Yohane 9:1-3

Chifukwa chiani ophunzira ake anafunsa ndikuti: “anachimwa ndani, ameneyo kapena atate wake ndi amake? Ndichifukwa chakuti anthu anali kukhulupirira kuti ngati china chake sichiri bwino ndiye kuti, mwina mwake; atate wako kapena mayi wako anachimwira Mulungu.

Mulungu anamuuza Ezekiel kuti achotse mwambi wakuti “Atate adya mphesa zosacha, ndi mano a ana ayayamira.” Ezekiel 18

- Ndipo anandidzera mau a Yehova, ndikuti, “mutani inu ndi kunena mwambi uwu za dziko la Israyeri, wakuti, atate adya mphesa zosacha, ndi mano a ana ayayamira.” Pali Ine, ati Ambuye Yehova, “simudzaonanso chifukwa chakunena mwambi uwu M’Israyeli.”

Pamene anthu ambiri lero amanena mwambi umenewu polumikiza chiphunzitso cha matemberero odzera magazi akumtundu. Mulungu adadana nawo mwambi umenewu ndikhulupirira kuti mpaka lero alikudana nawo. Mulungu anapitirira kunena kuti:

1) “Koma munthu akakhala olungama, nakachita chiweruzo ndi chilungamo, wosadya pamapiripo, wosakweza maso ake kumafano anyumba ya Israyeli, wosaipsa mkazi wa mnansi wake, kapena kuyandikira mkazi ataoloka, wosasautsa munthu aliyense, koma wambwezera wa ngongore chigwiriro chake, wosatenga zofunkha, anampatsa wanjara chakudya chake, nabveka wa mariseche ndi chobvala, wosapereka molipa phindu, wosatenga choonjezerapo wobweza dzanja lake lisachite zosalungama, woweruza zoona pakati pamunthu ndi nzake, amayenda m’malemba anga, nasunga maweruzo anga kuchita chokhulupirika; Iye ndiye wolungama adzakhala ndimoyo ndithu, anena Ambuye Yehova. (Ezekieli 18:5-9)

2) “Akabala mwana ndiye mkhungu, wokhetsa mwazi, wochita chimodzi cha ichi (ngakhale atate sanachita izi) wosachita zabwino zonsezija, koma anadyanso pamapiri, naipsa mkazi wa nansi wake, nasautsa osauka ndi osowa, natenga zofunkha zosabwezera chigwiriro, nakweza maso ake kumafano, nachita chonyansa, napereka molira phindu, nalandira choonjezerapo; adzakhala ndi moyo uyu kodi? Sadzakhala ndi moyo, anachita zonyansa izi zonse; kufa adzafadi mwazi wake unkhalira.” (Ezekieli 18:10-13)

3) “Taona tsono, yemweyo akabala mwana uyu, naona zochimwa zonse anachita atate wake, naopa osachita zoterozo, wosadya pa mapiri, kapena kukweza maso

ake kumafano anyumba ya Israyeli, wosaipsa mkazi wa mnansi wake, kapena kusautsa wina aliyense, wosatenga chigwiriro, wosatenga zofunkha; koma apatsa wosauka chakudya chake, nabveka wa mariseche ndi chobvala, naletsa dzanja lake pa wozunzika, wosalandira phindu kapena choonjezerapo, wochita maweruzo anga, nayenda m'malemba anga; uyu sadzafera mphulupulu ya atate ake, adzakhala ndi moyo ndithu." (Ezekieli 18:14-17)

Tsopano Mulungu analankhula kwa mibadwo yonse itatu kuti munthu aliyense ndi mdindo wa payekha wa moyo wake, siziri kukhuzana ndi zimene makolo ako anachita mbuyomu asanafe. Mau akuti:

- "Uyu sadzafera mphulupulu ya atate ake, adzakhala ndi moyo ndithu. Koma atate ake adzafa chifukwa cha machimo awo. Chifukwa anapembeza mafano, kubera m'bale wake, ndikuchita choipa pamaso pa anthu ake. Ndiye mwina m'kumafunsa chifukwa chiani Sali kugawana nawo mlandu wa atate ake? Pakuti mwanayu anachita cholungama, anasamalitsa kusunga malamulo a Mulungu, adzakhala ndi moyo. Moyo wochimwawo ndiye udzafa, mwana sadzasenza mphulupulu za atate ake, ndi atate sadzasenza mphulupulu za mwana, chilungamo cha wolungama chidzankhalira, ndi choipa cha oipa chidzankhalira. (Ezekieli 18:17-23)

Koma oipayo akabwerera kusiya machimo ake onse adawachita nakasunga malemba anga onse, ndikuchita chiweruzo ndi chilungamo, adzakhala ndi moyo ndithu sadzafa. Mnene chimodzi chonse chadzolakwa zake zonse adachita chidzakumbukika chimtsutse chilungamo chake anachita adzakhala ndi moyo. Ngati ndikondwera nayo imfa ya munthu woipa? Ati Ambuye Yehova, sindiko kuti abwerere kuleka njira yake ndikukhala ndi moyo? Ezekieli 18:17-23. Ndiye ngati wina akuonetsani Exsodo 20 kapena Deutronomy 9 kuti awonetsere kuti choipa cha atate chidzakhala pa wana kufikira m'badwo wa chitatu ndi wachinayi, ingowakumbutsani kuti "kwa iwo akudana ndi Mulungu." Mbuku la Ezekieli taona kuti zoipa za atate sidzidzafikira ana. Aliyense kudzankhalira kolingana ndi chilungamo chake kapena chosalungama chake. Chiphunzitso chakuti machismo atate adzakhala pa ana ndi chiphunzitso chonama. Tiri kukhala m'nthawi imene anthu ambiri ali kungokhulupira chiri chonse osasunga chiphunzitso choonadi, kwa iwo amati bola kukondana wina ndi nzake. Chiphunzitso choonadi ndichofunika kwambiri, Paulo anati pali ena amane amaphunzitsa zinthu zina amenewa ayenera aletsedwe.

- 1 Timoteo 1:3 … Monga ndinakudandaulira iwe utsalire mu Efeso popita ine Makedoniya, nditeronso, kuti ukalamulire ena asaphunzitse kanthu kena.

- 1 Timoteo 4:16 Udzipenyerere wekha, ndichiphunzitsocho, udzikhala mu izi pakuti pochita ichi udzadzipulumutsa iwe wekha ndi iwo akumva iwe.

- Tito 1: 9 Wogwira mau okhulupirika monga mwa chiphunzitso kuti akakhoze kuchenjeza mwa chiphunzitso cholamitsa, ndi kutsutsa otsutsana naye.

Tinapatsidwa mau a Mulungu kuti tikathe kutsutsana nawo iwo akuphunzitsa chinyengo Paulo akuti pali ena amene alikuyenda yenda ndikuphunzitsa zosocheretsa zakuononga chikhulupiriro cha ena. Zokhumudwitsa ndizakuti pamene ndinayang'ana pa internet pa kugwiritsa Google ndikulunjika za "matemberero amagazi, akumtundu" ndinapeza ziphunzitso zabwino pa ma website awiri mwa ma website makumi awiri kapena makumi atatu, ziphunzitso zina zonsezo zinali zopanda pake. Chinthu china chomvetsa chisoni ndichakuti Khristu achinyamata amapita ku mipingo imene imaphunzitsa ziphunzitso zotere. Banja lina linandiyimbira phoni kuti liri kupita kumpingo wotere wa ku Binoni. Tiyenera kusamala chifukwa izi siziri m'malemba, ndipo zimangobweretsa mantha m'mitima ya anthu. Paulo anamulembera Timoteo ndi kuti:

- "Pakuti Mulungu sanatipatsa mzimu wa mantha ;komatu wamphamvu ndi chikondi ndi chidziletso" (2 Timoteo 1:7)

Zinthu izi zimapeza malo mmalingaliro athu, tiyenera kukonzanso malingaliro athu kolingana ndi mmene Baibulo limanenera. Chilimbikitso changa abale, ndichakuti tiyeni tilowe mmalemba, osangolandira chirichonse chimene anthu alikuphunzitsa. Banjalija lina kalipiridwa chifukwa chotsutsa chiphunzitso cha matemberero akumtundu, chimene abusa ampingo umene iwo anapita anali kuchikhulupirira. Ndiri kukumbutsidwa chinthu china chokhuza mpingo wa ku Berea mu buku la Machitidwe 17 umene sunali kungokhulupirira chiri chonse munthu angaphunzitse koma unali kusanthula malamba kuti aone ngati chiphunzitsocho chinali kugwirizana ndi mau a Mulungu. Amenewa anali m'fulu koposa am'Tesalonika, popeza analandira mau ndi kufunitsitsa kwa mtima wonse, nasanthula malembo, masiku onse ngati zinthu zinali zinali zotero. (Machitidwe 17:11)

Muli ndi udindo ofufuza zimene ndiri kuphunzitsa. Muli ndi udindo ofufuzanso aliyense amene alikuphunzitsa mau aMulungu. Kaya ndi wotani, kaya ali ndi udindo wanji afufuzidwe. Ulamuliro wa Mau amulungu uli pamwamba pa zinthu zonse. Wonetsetsani ngati zilikugwirizana ndi mau aMulungu zilandireni koma ngati ziri kutsutsana ndi mau Musazilandire.

AUTHOR: Ken Paynter

- **For more ministry downloads visit:**
  http://www. agfbrakpan. co. za/ministry-archives. aspx

- **For more ministry downloads by Ken Paynter visit:**
  http://www. agfbrakpan. co. za/ministry-archives. aspx?speaker=Ken%20Paynter